## UNDUNA WA ZACHILENGEDWE, MPHAMVU ZA MAGETSI NDI MIGODI

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


# NYENGO MSABATAYI

## KUYAMBIRA PA 24 MPAKA PA 30 NOVEMBER, 2025

### NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Kuyambira mawa, Lolemba pa 25 November 2025, tiyembekezere nyengo ya mitambo ya patalipatali kuphatikizapo nyengo yofunda, komaso ya mvula ya mabingu yomwe izizagwa ya mphamvu m'madera ena ochepa makamaka a m'chigawo chaku m'mwera **monga mapu ali Kumanjawa akuonetsera. Mvula ikhala yochepa kuyerekeza ndi sabata yatha.**

*Mphepo ikuyembekezerekaso kumaomba ya mphamvu m'madera ena a mdziko muno makamaka a m'chigawo chaku mpoto.*





*Mapu akuonetsa mlingo wa mvula yomwe tikuyembekezera m'sabata ikubwerayi, kuphatikiza sabata yonse.*

### NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunali nyengo ya mphepo, yamitambo ndi ya mvula yamabingu yomwe inagwa yamphamvu m'madera ena**.** Mvula inagwa yambiri ku Vua ku Nkhata-Bay ndi mlingo wa **87.6mm** pa **21 November 2025.**

Mapu ali kumanja akuonetsa ina mwa mvula yomwe inagwa m'sabata yangothayi.




*Mapu akuonetsa kuchuluka kwa mlingo wa mvula m'sabata yangothayi*

### MALANGIZO M'SABATALI

- **Pomwe mvula yamphamvu ikuyembekezereka m'madera ena,** tiyeni tikonze njira zonse zodutsa madzi pochotsa zinyalala kuti tipewe madzi osefukira.
- **Mvula yamabingu:** Tikhale m'malo otetezeka
- **Kuziteteza ku Mphepo ya mkutho:** Tiyeni tionetsetse kuti nyumba zanthu ndi zofolera bwino.

***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 23 November, 2025**